CHARLES “CHIC” SHAVER

# TSOPANO PAKUTI NDINE MKHRISTU

## Maphunziro a Chidule a Achinyamata

Maphunziro a Chidule a Achinyamata
Charles “Chic” Shaver

Copyright © 2024
Nyumba Yosindikiza Mabuku ya Nazarene
Maphunziro awa anakozedwa ndi a Nazarene Youth International

Mark Gilroy, Mkozi
Janice J. Greeno, Mkozi Wothandizirat

Malemba onse atengedwa kuchokera Mu Mau a Mulungu m’Chichewa Chalero

# Malangizo kwa Wothandizira

Zikomo chifukwa chogwira ntchito ndi wokhulupirira watsopano!

Maphunziro awa akozedwa kuti mukhoza kupereka Phunziro limodzi sabata iliyonse. Mukhoza kusunga otsalawo kufikira mkumano wotsatira.

## 1. Cholinga cha maphunziro a Baibulo awa

Cholinga cha Phunziro ili ndi kuthandiza Akhristu atsopano kuti alandire thandizo, chitsogozo komanso chilimbikitso cha bwenzi la Chikhristu Udindo wanu ndikuphunzira Mawu a Mulungu pamodzi nawo, kupemphera nawo, ndipo khalani nawo ndi nthawi. Maphunziro awa akuthandizani kutero.

## 2. Kumananі mwachangu

Yesetsani kukumana ndi Mkhristu watsopano mwachangu, maka pasanathe maola 24 a kutembenuka mtima kwawo. Gwiritsani ntchito nthawi imeneyi kupemphera pamodzi. Kenaka apatseni Phunziro nambala 1 ndi vesi loloweza nambala 1 (dulani kuchokera ku pepala).

## 3. Konzekerani Phunziro lililonse

Santhulaninso Phunziro lililonse isafike nthawi. Ngati muli ndi mafunso ena aliwonse za mayankho olondola kapena matanthauzo a mavesi ena, kozani nthawi yokumana ndi abusa anu kapena mtsogoleri wa achinyamata kukambilana izi. Muli mpata mu Phunziro lililonse kuti Mkhristu watsopano alembemo mafunso ake. Ngati simungathe kuyankha, fusani abusa anu kapena mtsogoleri wa achinyamata.

## 4. Khazikitsani nthawi yokumana pafupipafupi

Ikani nthawi yokhazikika ya sabata iliyonse komanso malo okumaniranapo, maka pa nyumba ya wina, kwa masabata oposa asanu ndi atatu. Pa chigawo chilichose, bwerezaninso kuona Phunziro la m'mbuyo, tsimikizani kuti aloweza vesi loyenera kuloweza, ndipo kenaka apatseni Phunziro lotsatira komanso vesi. Bwerezani ndondomeko iyi kufikira maphunziro onse asanu ndi atatu atatha.

Ngati Mkhristu watsopano sanamalize Phunziro, khalani ndi nthawi yopangira Phunziro pamodzi.

## 5. Limbikitsani kukula kwa uzimu

Khalani ndi nthawi sabata iliyonse kuonelera kukula kwawo kwa ulendo wa uzimu. Alimbikitseni kulemba maganizo awo komanso zimene awona mu chigawo cha "Ulendo wanga wa uzimu". Khalani ndi nthawi ya mapemphero pamodzi. Ndondomeko ya Phunziro ili imatheka bwino ngati ubale wabwino ukhazikitsidwa pakati pa Mkhristu watsopano ndi m'phuzitsi.

## 6. Sungani mbiri ya m'mene kukumana kwanu kukuyendera

Gwiritsani ntchito "Kujambula kukuchitika." Ikatha nthawi ya Phunziro, fotokozani mwachidule mmene zinayendera. Izi zimakuthandizani kukumbukira zinthu zofunikira pemphero komanso zimapangitsa m'busa wanu kapena mtsogoleri wa achinyamata kudziwa mmene kupita patsogolo kwa Mkhristu watsopano kukukhalira.

## 7. Mutamaliza Phunziro lomaliza

- Perekani Setifiketi yoyenereza, yosayinidwa ndi inu koma abusa anu (kapena mtsogoleri wa achinyamata). Abusa akhoza kusankha kuperekera nanu pamodzi pa nthawi ya mwambo wa mapemphero.
- Perekani enivelopi ya mbiri ya Mayendedwe kwa abusa anu kapena mtsogoleri wa achinyamata kuti akhale ndi mbiri yanu.
- Kambiranani za chikozero cha kapitilizidwe ka kukula kwa makulidwe a uzimu. Alimbikitseni kutengapo mbali mu mpingo ndi gulu la achinyamata, ndi kuganizira kuyamba gulu laling'ono la maphunziro a Baibulo, mapemphero komanso kuchitira umboni.
- Khalani ndi nthawi kuyamika Ambuye chifukwa cha mwayi wothandiza wina wake kukula ngati wotsatira Yesu Khristu.

Dzina ______________________________________________ Tsiku ____________________

# Phunziro 1

# Kodi Chachitika kwa ine ndi Chiyani?

## Moyo weniweni

Mu nthawi yonse imene Jason anadziwa Damon, anasilira mmene Damon anakhalira. Damon anali osiyana ndi wina aliyense amene anakumanapo naye. Pamene makolo a Jason anathetsa ukwati, Damon anali pomwepo kumvetsera ndi kumuthandiza kuthetsa ululu kusiyana ndi m'nzake wina aliyense. Mu nthawi ina ya zokambirana zao, Damon ananena za mmene ubale wake ndi Yesu Khristu unabweretsera kusintha m'moyo wake. Anafunsa Jason ngati akufuna ubale wosintha moyo umenewu. Jason anavomera ndi kupemphera pemphero lachidule ndi Damon. Tsopano Jason anali ndi funso limodzi: "ndikudziwa kuti ndapemphera pemphero. Ndikudziwa china chake chasinthika, koma ndi chiyani kwenikweni chimene chachitika kuti ndisinthike?"

## Kusanthula Malemba

Pezani mayankho a mafunso awa mu Baibulo.

Ngati mulibe Baibulo, pali abwenzi ena a Chikhristu komanso mipingo imene ingakhale yokondwa kukuthandizani kuti mulipeze.

Mawu akanenedwa monga Yohane 1:12, zikutanthauza kuti mupite ku buku la Yohane, chaputala 1, vesi 12. Mndandanda wa mawu a mlozera wa Baibulo ufotokozera za tsamba la buku lililonse. Pezani yankho kuchokera mu Baibulo, kenaka lembani m'mawu anuanu.

1. Nditalandira Yesu pakuyitanidwa ndinakhala ______________________ wa Mulungu (*Yohane 1;12*).
2. Kubwera kwa Khristu m'moyo wa munthu ndi ubale wa payekha wonenedwa ndi Khristu mu Chivumbulutso 3:20.
   a. Kodi ndi ndani amene akugogoda pakhomo? (*Onani chivumbulutso 1:1 kuti muone chizindikiritso*) ____________
   ______________________________________________
   b. Kodi ndi ndani amene angavomere mawu ake komanso kugogoda kwake? ____________________
   c. Kodi akufuna kuti ine ndichite chiyani? ______________________________
   ______________________________________________
   d. Kodi adzachita chiyani ngati nditsegula khomo? ______________________________
   ______________________________________________
   e. Kodi ndingatsegule bwanji khomo? (*Onanl Chivumbulutso 3:19.*) ____________________
   ______________________________________________
   f. Kodi mwatsegula khomo? ______________________________________
   g. Kodi Yesu Khristu alikuti tsopano lino? ______________________________
   ______________________________________________
3. Kodi ndi chifukwa chiyani Khristu anadza kudzatifunafuna ndi kutipulumutsa ife? (*Luka 19:10*) ____________
   ______________________________________________
4. Monga mwa Aroma 3:23, kodi ndi chifukwa chiyani tinatayika? ______________________
   ______________________________________________
5. Kodi mphoto kapena malipiro a uchimo ndi chiyani, kolinga ndi Baibulo? (*Aroma 6:23*) ____________
   ______________________________________________
6. Kolingana ndi Aroma 5:8-9, kodi ndi ndani amene anafera kale machimo athu? (*Onani Yesaya 53:6 kuti mudziwe zambiri.*) __
7. Nditavomereza machimo anga kodi Mulungu anachita chiyani? (*1 Yohane 1:9*) (*Dziwani 1 Yohane, wotchedwa "Yohane woyamba ali kufupi ndi kumapeto kwa Chipangano Chatsopano. Ndi imodzi mwa makalata a Yohane ndipo ndi losiyana ndi buku la Uthenga Wabwino wa Yohane umene ukupezeka kufupi ndi kumayambiriro kwa Chipangano Chatsopano.*)____________
8. Lembani mzere kunsi kwa mau a ku Yesaya 55:7 amene amakuuzani zoyenera kuchita pa machimo olapa mowona mtima

   *"Woyipa asiye makhalidwe ake oyipa, ndipo wosalungama asinthe maganizo ake oyipa. Abwerere kwa Yehova, ndipo adzamuchitira chifundo,ndi kwa Mulungu wathu, pakuti adzamukhululukira koposa."*

9. Molingana ndi Aefeso 2:8-9, kodi timalandira chipulumutso motani? (Chongani pa bokosi logwirizana ndi yankho lolondora):
   - ☐ *a.* Kuchita zinthu zabwino zochuluka
   - ☐ *b.* Kuyesetsa kuti ndichite zoyenera
   - ☐ *c.* Kuvomereza chikhulukiro cha Mulungu mwa chikhulupiriro

10. Tikalandira chipulumutso ndikukhala wolengedwa mwatsopano mwa Khristu, Kodi Cholinga cha Mulungu pa ife ndi chiyani? (*Aefeso 2:10*) ______

11. Kodi ndikudzera mwa ndani mmene timafikira podziwa Mulungu? (*Yohane 14:6, 9*) ______

12. Werengani 1 Yohane 5:13. Kodi chidzachitika ndi chiyani kwa iwo amene amakhulupirira Yesu Khristu, mwana wa Mulungu?
   - ☐ *a.* Amayembekezera kukhala ndi moyo wosatha
   - ☐ *b.* Amaganiza kuti akhoza kukhala ndi moyo wosatha
   - ☐ *c.* Amadziwa motsimikizika kuti ali ndi moyo wosatha

13. Nditati ndafa usiku uno, kodi ndipita kuti? (Yohane 6:45-47) ______

______

## Mafunso anga okhudza Phunziro ili

______

______

______

______

## Zofunika kuchita pa moyo

1. Lembani chiganizo chachifupi chofotokozera mmene mukudziwira kuti ndinu mwana wa Mulungu.______

   ______

   ______

2. Tsopano pakuti ndabadwanso mwauzimu ndipo ndine mwana wa Mulungu (*Yohane 3:3-7*), ndifunika chakudya cha uzimu kuti ndikule. Kodi chofunikira kwambiri mu chakudya changa ndi chiyani? (*Mateyu 4:4*) ______

   ______

### ***Mmusimu muli malangizo abwino. Chongani lililonse pamene mukuwachita:***

- ☐ Werengani Baibulo lanu tsiku ndi tsiku. Ndicho choyambirira mu chakudya chanu. Khazikitsani nthawi tsiku ndi tsiku. Yambani ndi uthenga wa Yohane—chaputala chimodzi kapena kapena ndime zochepa tsiku lililonse. Mafunso ambiri mu "Kusanthula Malemba" amachokera mu Yohane.
- ☐ Pempherani tsiku ndi tsiku. Yankhulani ndi Mulungu kuchokera pansi pa mtima wanu.
- ☐ Pitani ku Tchalitchi paliponse pamene pali kuthekera. Onetsetsani kuti ndi mpingo umene umalalikira Baibulo ndi kukweza Khristu.
- ☐ Lowezani malemba. Masalmo 119:11 amati, "Ndasunga mawu anu mu mtima mwanga kuti ndisakuchimwireni." Kuloweza malemba kumatithandiza kumvera Mulungu. Khalani owonetsetsa kuloweza vesi la Phunziro lililonse.
- ☐ Mverani Mulungu. Ngati simuli otsimikizika kuti Chinachake ndi cholondola kapena cholakwika, dzifunseni "Yesu akanachita chiyani?"
- ☐ Chitirani umboni. Uzani wina wake zimene Ambuye wakuchitiranani.

## Vesi loloweza

*"Taonani ndaima pakhomo ndikugogoda. Ngati wina amva mawu anga natsekula chitseko, Ine ndidzalowamo, ndi kudya naye, Ine ndi iyeyo." (Chivumbulutso 3:20)*

## Zolemba zanga za uzimu

______

______

______

Tsopano muli ndi kumvetsetsa kwabwino kwa "Zimene zandichitikira." Koma, ichi ndi chiyambi chabe cha zinthu zazikulu—pali zachuluka.

Dzina ______________________________________________ Tsiku ___________________

# Phunziro 2

## Kuyenda ndi Mulungu

### Moyo weniweni

Jason akumva kuperewera. Posachedwapa anasanduka Mkhristu, ndipo waona kusinthika kwina kwakukulu m'moyo mwake. Koma akusawutsikabe ndi malingaliro ake komansozochitika zake. Akumva chisoni chifukwa chowilingulira amayi ake atamupempha kachitatu kuti agwire ntchito. Jason akudabwa, "Kodi ukakhala Mkhristu, umakhala bwanji ngati Mkhristu?" Mwina munadzifunsapo funso lotere.

Mwana akabadwa mwathupi, amafunika kuyamba kukula, kuphatikizapo kuphunzira kuyenda. Chimodzimodzi za uzimu. Mwana wa Mulungu amaphunzira kuyenda ndi Mulungu—gawo limodzi panthawi.

### Kusanthula Malemba

1. Pamene mukuwenga Uthenga Wabwino wa Yohane, mukhoza kuwona zichitochito zina zimene zimatanthauza chimodzimodzi ngati kuyenda ndi Mulungu. Kodi zina mwa izo ndi chiyani?
   a. Yohane 8:12 ______________________
   b. Yohane 1:37 ______________________
   c. Yohane 2:5 ______________________
   d. Yohane 5:14 ______________________
2. Kodi ndi ndani amene amalimbana ndi kuyenda kwathu ndi Mulungu? (*1 Petro 5:8*) ______________________
3. Kodi mdyerekezi anachita chiyani mu Mateyu 4:1? ______________________
4. Kodi Yesu anagonjera yesero? (*Aheberi 4:15*) ______________________ Kodi mayesero ndi tchimo ndi zofanana? ______________________
   (Yesero limafunsa, "Kodi utero?" Tchimo limati, "Nditero" —ndikuchita.
5. Kodi tiyenera kuchita chiyani mdyierekezi akatigwira? (*Yakobo 4:7*) ______________________
6. Yesaya 59:2 amati, "Koma zoipa zanu zakulekenetsani ndi Mulungu wanga ndipo wakufulamirani chifukwa cha machimo anu, kotero Iye sadzamva." Chinthu chokhacho chimene chingandisiyanitse ndi Mulungu ndi chiyani? ______________________
7. Kodi Mkhristu, kudzera mu mphamvu ya Khristu, angapewe kuchimwa kwa dala? (*1 Yohane 3:9*) ______________________
8. Ngati Mkhristu wachimwa, ayenera kuchita chiyani molingana ndi 1 Yohane 2:1? (Chongani yankho lolondola)
   - ☐ *a.* Anene kuti sangachitire mwina koma kuchimwa.
   - ☐ *b.* Kubisa machimo awo ndikukhala ngati palibe chimene chachika.
   - ☐ *c.* Apite kwa Yesu Khristu nthawi yomweyo, kuvomereza tchimo, ndi kupitiriza kukhala ndi Mulungu.
9. Ngati Mkhristu wachimwa ndi kuvomereza. Kodi Mulungu adzachita chiyani? (*1 Yohane 1:9*) ______________________
10. Molingana ndi Yohane 14:21, kodi kusunga malamulo a Khristu kumawonetsa chiyani? ______________________
11. Werengani Yohane 10:27-29 ndipo yankhani mafunso awa:
    a. Kodi ndi ndani amene ali ndi moyo wosatha ndipo ndi wotetezedwa ndi mphamvu ya Mulungu? ______________________

b. Kukhala nkhosa ya Khristu (vesi 27), ndiyenera kumva Mawu Ake, kudziwika ndi Iye, komanso china ndi chiyani? ______________________________

## Mafunso anga okhudza Phunziro ili

______________________________

## Zofunika kuchitapo kanthu

1. Ndimayenda ndi Mulungu! Izi zitanthaiza kukana yesero; kumvera Mulungu, komanso kutsata Yesu. Mulungu amalonjeza kuti pamene tiyesedwa, adzatipangira njira kuti tithawirepo kapena kupirira. (*1 Akorinto 10:13*)
2. M'mau anu, fotokozerani kuti tchimo ndi chiyani (*1 Yohane 3:4 ndi Yakobo 4:17*). ______________________________
3. Kodi ndi dera kapena madera ati a moyo wanu amene mumamva kuyesedwa Kwambiri? ______________________________
4. Kodi ndi ndondomeko yanu yotani ya kukana mayesero ndi kumvera Mulungu? ______________________________

### Vesi loloweza

*Palibe mayesero amene mwakumana nawo oposa amene anthu ena onse anakumana nawo. Mulungu ngokhulupirika; sadzalola kuti inu muyesedwe koposa muyeso umene mutha kupirira. Koma pamene pamene mwayesedwa, Iyenso adzakupatsani njira yopambanira mayeserowo. (1 Akorinto 10:13)*

## Zolemba zanga za uzimu

______________________________

Kuti mupeze ndondomeko za chikhalidwe cha Chikhristu ndi kukula zikupezeka mu Phunziro lotsatira. Iyi ndi njira yokozedwanso komanso yothyakuka bwino ya Phunziro 3:

Dzina ______________________________ Tsiku ______________

# Phunziro 3

## Kuphunzira kuchokera kwa Mulungu

### Moyo weniweni

Jason siyekhayo amene akuphunzira za mmene angakhalire moyo wa Chikhristu. Janice, amene wakhala akupita komansokujomba ku tchalitchi anasunthika kwambiri ndi zimene zinachitika kwa Jason kuti anapempha Mulungu kuti amukhululukire ndi kudziperekanso mwatsopano kuti achite chifuniro chake. Funso lake lalikulu tsopano lakhala lakuti "Ndi ziyangoyango zochuluka za zabwino ndi zoipa, kodi ndingadziwe bwanji zimene Mulungu amayembekezera kuchokera kwa ine? Kodi ndingadziwe bwanji chimene chili choonadi?"

Ndingadziwe bwanji chimene chili choona? "Kusanthula Malemba" uku kukuonetsani ku chiyambi chopezera chifuniro cha Mulungu.

### Kusanthula Malemba

1. Werengani Yohane 17:17. Kodi akufotokozera Mau a Mulungu motani? (Baibulo)? ______________
______________________________
2. How was the Scripture given to us to guarantee its truth? (*2 Timothy 3:16*) ______________
______________________________
3. Kodi Mau a Mulungu adzachita chiyani kwa ife molingana ndi:
   a. 2 Timoteyo 3:14-15 ______________
   b. Yohane 15:3 ______________
   c. Machitidwe 20:32 ______________
4. Pamene mukuwenga Uthenga Wabwino wa Yohane, mukhoza kuwona ziphunzitso za ubwino wa Mau a Mulungu:
   a. Kodi Yesu Khristu anachita chiyani ndi Mau (malamulo) a Atate ake? (*Yohane 8; 55*) ______________
   ______________________________
   b. Kodi ndi malo otani amene Mau a Mulungu (uthenga wa choonadi) amachita m'miyoyo ya anthu ena? (*Yohane 8:37*) _
   ______________________________
   c. Ngati tili ake a Mulungu, tidzachita chiyani za Mau ake? (*Yohane 8:47*)______________
   ______________________________
   d. Kodi ophunzira weniweni wa Khristu adzachita chiyani ndi Mau a Mulungu (vumbulutso kapena chiphunzitso)? (*Yohane 8:31*) ______________
   ______________________________
   e. Kodi tiyenera kuchita chiyani ndi Mawu (lamulo, chiphunzitso kapena zonena) kuti tisungebe moyo wa uzimu komanso wosatha? (*Yohane 8:51*)______________
   ______________________________
5. Ngati ndimakonda Khristu, kodi ndidzachita chiyani? (*Yohane 14:23*) ______________
______________________________
6. Werengani Yohane 20:31. Kodi ndi chifukwa chiyani Mau a Mulungu analembedwa? ______________
Kodi ndi mphatso yotani imene ndingalandire ngati ndikhulupirira izi? ______________
7. Mdyierekezi akhoza kufuna kutigonjetsa, koma Mulungu watipatsa chida chomugonjetsera. Ichi ndi "lupanga la Mzimu," limene lili chiyani? (*Aefeso 6:17*) ______________
______________________________
8. Kodi anamukaniza bwanji mdyierekezi pa Mateyu 4:4, 7, 10? ______________
______________________________

9. Molingana ndi Masalmo 119:11, kodi ndingachite chiyani ndi Mau a Mulungu kuti ndisamuchimwire? ________________
_____________________________________________

## Mafunso anga aphunziro ili

_____________________________________________
_____________________________________________
_____________________________________________
_____________________________________________

## Zofunikira kuchitapo kanthu

1. Ndi choonadi chiti chochokera ku Mau a Mulungu chimene chakuthandizani posachedwapa? ________________
_____________________________________________
_____________________________________________

2. Kodi ndi chifukwa chiyani Mkhristu akuyenera kuwerenga Baibulo tsiku ndi tsiku? ________________
_____________________________________________
_____________________________________________

## Vesi loloweza

*"Ndasunga mau anu mu mtima mwanga kuti ndisakuchimwireni." (Masalmo 119:11)*

## Ulendo wanga wa uzimu

_____________________________________________
_____________________________________________
_____________________________________________
_____________________________________________
_____________________________________________
_____________________________________________
_____________________________________________
_____________________________________________
_____________________________________________
_____________________________________________
_____________________________________________
_____________________________________________
_____________________________________________
_____________________________________________

Kupitirira "pa kuphunzira kuchokera kwa Mulungu" Muli ndi mwayi wina wodabwitsa ngati Mkhristu. Zavumbulutsidwa mu Phunziro lotsatira.

Dzina ______________________ Tsiku ____________

# Phunziro 4

## Kuyankhula ndi Mulungu

### Moyo weneweni

"Kkodi Mulungu motani amene sungathe kumuona?" "Jason anavomereza kuti Marko, amene ndi nzake, anafunsa funso labwino. Mwezi watha womwewu, Jason akanakhala kuti ndiye amafunsa. Tsopano ngati Mkhristu watsopano, iye akuyesetsa kuyankha. Koma pali nthawi zina amamva kuti mapemphero ake ndi Mau chabe. Jason akudwabwa, ungalankhure bwanji kwa Mulungu amene siukumuona, ndipo ungalongosolere bwanji izi kwa mzako?"

Wolemba Masalmo anati: "Mmawa, Yehova mumamva mawu anga; m'mawa ndimayala zopempha zanga pamaso panu ndi kudikira mwachiyembekezo" (Masalmo 5:3). Tiyeni tisanthule mozama malangizo ena amene Baibulo limatipatsa za chida chotchedwa "pemphero".

### Kusanthula Malemba

1. Kodi Yesu anakhulupilira kukhala ndi nthawi ya payekha ya pemphero ndi Atate Ake? (*Marko 1:35*) ____________
2. Kodi ndipemphere liti? (*Luka 18:1*) ____________
3. Kodi ndi malingaliro otani kapena zochita zotani zimene ziyenera kukhala mbali ya pemphero? (*1 Atesalonika 5:17-18*) ____________
4. Kodi chopangitsa chachikulu cha pemphero losayankhidwa, ndi chiyani molingana ndi Masalmo 66:18? ____________
5. Kodi ndi chiyani chimene chiyenera kukhala chitsimikiziro cha zimene tikupempherera? (*1 Yohane 5:14*) ____________
6. Kodi mwaphunzira zinthu zina kuchokera mu buku la Yohane zokhudza pemphero?
   a. Kodi ndi mwayi wotani umene Mkhristu aliyense alinawo? (*Yohane 16:24*) ____________
   b. Kodi cholinga cha Mulungu pa kuyankha pemphero ndi chiyani? (*Yohane 14:13*) ____________
   c. Kodi Khristu amafuna chiyani kwa ife kuti ayankhe zopempha zathu? (*Yohane 15:7*) ____________
7. Kuti ndilandire yankho, ndiyenera kuchita chiyani ndikamapemphera? (*Mateyu 21:22*) ____________
8. Kodi ndi zinthu zina ziti zimene ndingapempherere?
   a. Mateyu 6:11 ____________
   b. Mateyu 9:38 ____________
   c. Afilipi 1:9 ____________
   d. 1 Timoteyo 2:1-2 ____________
   e. Yakobo 1:5 ____________
9. Kodi ndi chiyani chingalepheretse Akhristu kuti "asachimwe pamene ayesedwa." (*Mateyu 26:41*) ____________

10. Mapemphero abwino ndi amene amachita chiyani? (Chongani yankho lolondola)
   - ☐ *a.* Kugwiritsa ntchito , mau okhozeka a chipembedzo
   - ☐ *b.* Kuoneka bwino komanso osamalika
   - ☐ *c.* Ochokera pansi pa mtima

## Mafunso anga okhudza Phunziro ili

______________________________
______________________________
______________________________
______________________________

## Zofunika kuchitapo kanthu

1. Nenani zinthu zina zimene mukufuna kuyankhula kwa Mulungu za izo (za banja, abwenzi, Sukulu, ntchito ya ku Sukulu, ndi zina zotero).
   ______________________________
   ______________________________
   ______________________________

2. Kodi mudakhazikitsa kale nthawi ya pemphero? Ngakhale kuti mukhoza kufuna kupemphera tsiku lonse, kodi ndi nthawi yanji komanso malo ati amene mungakonde opemphererapo mwapadera tsiku ndi tsiku. ______________
   ______________________________
   ______________________________
   ______________________________

## Vesi loloweza

*"Mpaka tsopano simunapemphe kalikonse m'dzina langa. Pemphani ndipo mudzalandira, ndipo chimwemwe chanu chidzakhala chathunthu." (Yohane 16:24)*

## Ulendo wanga wa uzimu

______________________________
______________________________
______________________________
______________________________
______________________________
______________________________
______________________________
______________________________
______________________________
______________________________
______________________________
______________________________
______________________________
______________________________
______________________________

Mwina simunazindikire kukula kwa mwayi woyankhula ndi Mulungu wamphamvu yonse. Chikondi chonse komanso madalitso amene wakuonetsani chimakutakasani kuti mumuchitire Chinachake, sichoncho?

Dzina ______________________________ Tsiku ______________

# Phunziro 5

## Kugawana ndi Mulungu

### Moyo weniweni

Abwenzi asanu ndi atatu akhala akukumana lachiwiri lililonse ku madzulo kwa miyezi inayi tsopano. Damon, Jason, Janice ndi anthu ena asanu anapanga gulu lopemphera, kuphunzira Baibulo ndi kulimbikitsa kukula kwa uzimu kwa wina ndi mnzake. Pamkumano wawo wapitawu pemphero la Angela linatumphuka. Wavutika kuti amve kupezeka kwa Mulungu koma posachedwapa anawona chipambano. Anapemphera kuti "Mulungu, ndikukhulupirira mwa inu tsopano, kuposa kale! Ndikufuna ndikukondweretseni, kukutumikirani ndi kudzipereka zonse zimene ndili komanso zimene ndili nazo ndi inu."

Mtumwi Paulo anawonetsa maganizo ofanana: "Ndi chifukwa chake chilichonse mungadye kapena kumwa, kapena chimene mungachite, chitani zonse ku ulemerero wa Mulungu." (1 Akorinto 10:31). This Study explores how this truth applies to each of us.

### Kusanthula Malemba

1. Molingana ndi Mateyu 22:36-40:
   a. Kodi ndiyenera kukonda Mulungu motani? ______________
   b. Kodi ndiyenera kukonda m'nasi wanga motani? ______________
2. Kodi ndingawonetsere chikondi motani kwa Mulungu komanso ena? (*1 Yohane 5:2-3*) ______________
   ______________
3. Kodi Yesu ananena chiyani za kudzipereka kwa thunthu kwa Mulungu komanso zimene Iye adzachita.
   a. Kuti mbeu ya tirigu ibweretse zokolola zochuluka iyenera itani? (*Yohane 12:24-25*) ______________
   b. Ngati ndimatumikira Yesu Khristu, m'malo mwa zikhumbokhumbo zodzikonda, kodi Atate adzachita chiyani? (*Yohane 12:26*)______________
4. Ngati Mkhristu, ndili ndi malingaliro atsopano pa ubale wa m'moyo chifukwa ubale wanga watsopano ndi Mulungu. Pamene ndili "mwa Khristu" (Mkhristu, woyanjana naye), zakale zakonzedwa ndi chiyani? (*2 Akorinto 5:17*) ______________
   ______________
   a. Ubale wanga watsopano pa katundu:
      1) Tsopano ndikufuna [kupereka] [kusunga] zinthu. (Zungulizani mau oyenera) (Luka 6:38).
      2) Chongani maganizo atatu oyenera pa zinthu, zonenedwa pa Aefeso 4:28:
         - ☐ Kusabanso.
         - ☐ Kugwira ntchito molimbikira.
         - ☐ Kutenga zimene ndingathe.
         - ☐ Kugawana ndi osowa.
         - ☐ Malingaliro anga siwofunikira.
         - ☐ Kukhazikika pa zokhazo zimene zili zabwino.
   b. Ubale wanga watsopano pa ena:
      1) Kodi ndiyenera kukhala otani kwa anthu ena? (*Aefeso 4:32*) ______________
         ______________
      2) Ndiyenera [kupewa] kapena [kufunafuna] ubale wabwino ndi anthu amene si Akhristu kuti ndikhale moyo wa thunthu wolungama (*2 Akorinto 6:14*).
   c. Ubale wanga kwa ine mwini:
      1) Pakusamalira ndi kugwiritsa ntchito thupi langa, ndiyenera kukumbukira kuti ndi chiyani? (*1 Akorinto 6:19*) ______________
         ______________
      2) Kodi ndiyenera kuchita chiyani ndi nthawi yanga komanso mwayi? (*Aefeso 5:15-16*) ______________

5. Ndiyenera kukonda ______________________________ (*1 Yohane 2:10*), koma ndisakonde ______________________________ (*1 Yohane 2:15-16*).
6. Kodi ndi chifukwa chiyani Mulungu amayembekezera ife kumulemekeza? (*1 Akorinto 6:20*) ______________________________
7. Kodi zotsatira zake ndi chiyani ngati ndipanga ufumu wa Mulungu kukhala mbali yofunikira pamoyo wanga? Pamene (Mulungu akulamulira moyo wanga mwathunthu)? (*Mateyu 6:31-33*) ______________________________
8. Tikamagawana miyoyo yathu ndi Mulungu pakubwezera chikondi chake, kodi ndi ndani amene amalandira zochuluka? (*Marko 10:28-30*) ______________________________

### Mafunso anga a Phunziro ili

______________________________

## Zofunika kuchitapo kanthu

Pali njira zambiri zimene munthu angagawirane yekha ndi Mulungu. Nenani njira zisanu zapadera zimene mungagawirane nokha ndi Mulungu:

1. ______________________________
2. ______________________________
3. ______________________________
4. ______________________________
5. ______________________________

### Vesi loloweza

*N'chifukwa chake chilichonse mungadye kapena kumwa, kapena chimene mungachite, chitani zonse ku ulemerero wa Mulungu. (1 Akorinto 10:31)*

## Ulendo wanga wa uzimu

______________________________

Taphunzira kuti muli chimwemwe mkugawana ndi Mulungu. Palinso mtundu wina wakugawana tikamayankhula za Khristu kwa ena, kotchedwa kuchitira umboni. Phunziro lotsatira linena za zimenezi.

Dzina ______________________________ Tsiku ______________

# Phunziro 6

## Kugawa chikhulupiriro changa

### Moyo weniweni

Angela wapeza chimwemwe m'moyo mwake chimene samadziwa kuti ndi zotheka kufikira atadzipereka kwathunthu kwa Mulungu. Akuzindikira kuti enanso akufunikira kusinthika kwa mtima kumene analandira – mchimwene wamkulu Carl. Angela akudandaula chifukwa cha abwenzi ake a Carl komanso khalidwe lake. "Sindikudziwa kuti ndimuuze chiyani kapena kufotokozera mmene Mulungu wasinthira moyo wanga." Akuuza anzake wopemphera nawo. "Koma mukandipempherera, ndikukhulupirira kuti Mulungu andiwonetsa njira yomufikilira."

Angela anaphunzira kale Phunziro lofunikira: anthu ambiri amawona kusinthika kwakukulu kudzera mwa Yesu koma safuna kuwuza ena. Kuchitira umboni ndikuuza ena zimene Khristu wakuchitirani.

### Kusanthula Malemba

1. Khristu atachiritsa munthu wodzala ndi ziwanda, anamupatsa lamulo lapaderadera. Kodi tanthauzo lanji la "kuchitira umboni" limene mukulipeza apa? (*Luka 8:39*) ______________________________

2. Uthenga Wabwino wa Yohane umaphunzitsa zambiri za kuchitira umboni:
   a. Kuchitira umboni (kapena kuperekera umboni) ndi kugawira (sankhani chimodzi):
      - ☐ *a.* Zimene mwakhala mukuphuzitsidwa ndi choonadi.
      - ☐ *b.* Chimene mwamva kuchokera kwa wina wake.
      - ☐ *c.* Zimene mwawona ndi kumva – chodzidziwira nokha. (*Yohane 3:32*)

   b. Kodi Andreya amachita chiyani pa Yohane 1:40-41? ______________________________

   c. Kodi ndi "ntchito "yanji imene Yesu amati kuti Mulungu amafuna tizichita? (*Yohane 6:28-29*) ______________________________

   d. Kodi Yesu akutiwuza kuti tizichita chiyani pa Yohane 15:16? ______________________________

3. Ngati kukhala Mkhristu ndi chinthu chachikulu chakuti sichinachitikepo kwa inu, kodi ndi mphatso yayikulu bwanji imene mungapereke kwa munthu wina? ______________________________

4. Kodi Yesu akutilamula kuchita chiyani pa Mateyu 28:18-20? ______________________________

5. Kodi Akhristu oyambirira amawonetsa motani kuti avomereza Khristu? (Machitidwe 8:12, 35-38) ______________________________

   Kodi munapanga kuwonetsera uku kwa chikhulupiriro? (Onani chilichose chimene chikugwirizana)

   ☐ Inde ☐ Ndikuganizira

   ☐ Ayi ☐ Sindimadziwa

6. Kodi moyo wa iwo amene sakhulupirira Khristu ndi otani? (*Yohane 3:18*) ______________________________

7. Ngati ndimatsata Khristu, kodi akunena kuti adzachita chiyani? (*Mateyu 4:19*) ______________________________

8. Molingana ndi 1 Petro 3:15, kodi ndingadzikozekeretse motani kuti ndichitire umboni za Khristu? ______________________________

9. Kodi Paulo anakumana nawo kuti anthu kukagawana Uthenga Wabwino wa Khristu? (*Machitidwe 17:17*) ______________________________

10. Kodi ndi chifukwa chiyani uthenga wathu uyenera ulunjike pa Khristu? (*Yohane 14:6*) ______________________________

11. Ngati mboni, kodi uthenga wathu uyenera kukhala wotani?
Yohane 3:16
Aroma 6:23
Aroma 3:23
Yesaya 53:6
Yohane 1:12

12. Munthu akalandira Khristu, kodi udindo wathu ndi otani pa iwo? (*Machidwe 14:21-22*)

## Mafunso anga a Phunziro ili

## Zofunika kuchitapo kanthu

1. Kuchitira umboni kumakhala ndi mbali zitatu. (1) Moyo wanga ndisanakhale Mkhristu; (2) Mmene ndinakhalira Mkhristu; (3) Zimene Khristu wakhalira m'moyo mwanga. Lembani umboni waufupi umene mungagawane ndi mzanu.

2. Tchulani maina atatu a anthu amene mumawadziwa amene akufunika Khristu. Apemphereni ndipo funani mwayi owachitira umboni.
   1.
   2.
   3.

### Vesi loloweza

*Yesu anati, "Bwerani, tsateni Ine ndipo ndidzakusandutsani asodzi a anthu." (Mateyu 4:19)*

## Ulendo wanga wa uzimu

Tsopano pakuti mukudziwa kuti muyenera kuwuza ena za Yesu Khristu, mukhoza kuchita mantha kutero. Kodi mudzaipeza kuti mphamvu yoyankhulira posatengera mantha anu? Izi ndi zimene phunziro lotsatira lifotokozere.

Dzina ______________________________ Tsiku ______________

# Phunziro 7

## Kudzazidwa ndi Mzimu

### Moyo weniweni

“Ambuye mukudziwa mmene ndimafunira kukhala nanu. Pepani chifukwa moyo wanga umakhala wopelewera nthawi zambiri. Ndikufunitsitsa kuti ndikusangalatseni. Ndikufuna kuti ndizindikiritse ena za zimene zimatanthauza kutsatira inu. Ndikufuna kulimbika mtima kochitira umboni m’dzina lanu. Koma ndikuoneka kuti ndikulephera. “Kodi chilipo chimene chikusowekera m’moyo wanga, Ambuye?” Ili ndi pemphero la Jason lowona.

Jason siyekhayo amene ali ndi kumva kwakuti akufuna kuchitira Ambuye zochuluka koma akusowekera mphamvu. Yankho la vuto ili ndi lowonekeratu: Tikuyenera kukhala ndi mphamvu yochuluka ya Mulungu kudzera mwa Mzimu Wake. Ndi chifukwa chake Paulo analangiza Akhristu a m’nthawi yake kuti “adzazidwe ndi Mzimu” (Aefeso 5:18).

### Kusanthula Malemba

1. Yesu anakhala ndi nthawi yochuluka kuphunzitsa ophunzira Ake za Mzimu Woyera. Yohane analemba china mwa chiphunzitso chimenechi:

   a. Kodi ndi ndani amene Yesu ananena kuti adzatipatsa kusefukira ndi Mulungu (ngati mitsinje ya madzi a moyo)? (*Yohane 7: 37-38*) ______________________________

   ______________________________

   b. Kodi ndi ndani amene adzatiphuzitsa? (*Yohane 14:26*) ______________________________

   c. Mzimu wa choonadi amachitira umboni za ndani? (*Yohane 15:26*) ______________________________

   d. Kodi ndi pamsinkhu uti wa uzimu pamene Mzimu Woyera amakhala kuti wayamba kugwira ntchito? (*Yohane 3:5*) ____

   ______________________________

2. Kodi ndi kuchokera kwa ndani kumene ophunzira a Khristu afunika kulandira mphamvu yoyenera kuti achitire umboni? (*Machitidwe 1:8*) ______________________________

   ______________________________

3. Kodi Sauli (Paulo) anafunikira chiyani cha uzimu, ngakhale pambuyo pakuvomereza Khristu? (*Machitidwe 9:17*) _________

   ______________________________

   ______________________________

4. Maumboni a kusowekera kwa kudzazidwa ndi Mzimu kumpingo wa kwa Akorinto anawonetsa maganizidwe olakwika, monga kaduka, kusonyeza kuti adali akadali otani? (*1 Akorinto 3:1, 3*) ______________________________

   ______________________________

5. Kodi ntchito yapaderadera ya Mzimu Woyera imene imatiyeretsa ndikutipatuliratu kwathunthu ndi iti? (*1 Petro 1:2*) ____

   ______________________________

6. Kodi Yesu anapempherera chiyani kwa ophunzira Ake? (*Yohane 17:17*) ______________________________

   ______________________________

7. Pamene Mulungu Anapereka Mzimu Woyera kwa Akhristu oyambirira, kodi anachita chiyani ndi mitima yawo yosayeretsedwa? (*Machitidwe 15:8-9*) ______________________________

8. Kodi tiyenera kuchita chiyani ndi dera lina lililonse m’miyoyo yathu limene lili lodetsedwa? (*2 Akorinto 7:1*) ___________

   ______________________________

9. Kodi ndi uthunthu wa chiyero chathu wotani umene Mulungu amafuna ukhale? (Mamasulilidwe ena a Baibulo akhoza kugwiritsa ntchito mau osiyana a chiganizo chomwecho: “kuyera” “kuyeretsa” kapena “kupatula “) (*1 Atesalonoka 5:23*) _

   ______________________________

10. Kodi ndi ndani amene adzandiyeretsa “kotheratu”? (*1 Atesalonika 5:23*) ______________________________

    ______________________________

11. Lamulo la ______________________________ limandimasula ku “lamulo la uchimo ndi imfa.” (*Aroma 8:2*) ______________________________

12. Machitidwe olakwika a Akorinto anawonetsa kuti anasowekera khalidwe lotani lofunikira la moyo wa Chikhristu? (*1 Akorinto 13:13*) ____________________
____________________

13. Ndikhoza kulandira chikondi cha Mulungu kuchokera ____________________ (*Aroma 5:5*).

14. Nditadzazidwa ndi Mzimu Woyera, ndisakhalenso monga mwa ____________________, koma monga mwa ____________________ (*Aroma 8:4-5*).

### Mafunso anga ophunzira ili

____________________
____________________
____________________
____________________

## Zofunika kuchitapo kanthu

1. Kodi ubale wanga ndi Mzimu Woyera ndi wotani tsopano lino?

____________________
____________________
____________________
____________________

2. Moyo woyeretsedwa komanso wopatsidwa mphamvu wa Chikhristu ndi umene uli wodzazidwa ndi Mzimu wosefukira kwa ena.

- ☐ Pemphani Mulungu kuti akupatseni Mzimu mu chidzalo chake. (Luka 11:13).
- ☐ Perekani moyo wanu wonse kwa Mulungu. (Aroma 12:1-2).
- ☐ Vomerezani zakufunika kwanu kwa kuyeretsedwa kwa mkati. (Machitidwe 15:8-9).
- ☐ Landirani Mzimu Woyeretsa mwachikhulupiliro. (Machitidwe 15:8-9, 1 Atesalonika 5:23-24).

### Vesi loloweza

*"Mulungu mwini, Mulungu wamtendere, akuyeretseni kotheratu. Mzimu wanu wonse, moyo ndi thupi zisungidwe zopanda cholakwa mpaka kubwera kwa Ambuye athu Yesu Khristu" (1 Atesalonika 5:23)*

## Zolemba zanga za uzimu

____________________
____________________
____________________
____________________
____________________
____________________
____________________
____________________
____________________
____________________
____________________

Tikuyamikira pakupita chitsogolo kumene mwapanga m'maphunziro awa komanso m'kuyenda kwanu kwa Chikhristu. Musasiye tsopano! Ndipo kumbukirani kuti simulimo nokha. Phunziro lotsatira linena za izi.

Dzina ______________________________ Tsiku ______________

# Phunziro 8

## Mbali ya banja

### Kusanthula Malemba

Jason wapeza abale. Damon, Janice, ndi Angela ndi mbali ya banja limeneli. Zosadabwitsa, ndi anzake a tsinkhu umodzi, amapita Sukulu imodzi, ndipo amagawana zambiri. Koma, banja limene Jason wapeza ndi lokulirapo komanso lozama kuposa ubwenzi wamba. Komanso akumva kulumikizika bwino ndi ena a ku tchalitchi kwatsopano, monga, agogo achikulire a Reed a zaka 80, ndi Jimmy wa zaka 7. Zimene Jason wapeza ndi zakuti pamene anakhala Mkristu, Mkhristu aliyense owona, anakhala m'bale kapena mlongo wake. Chimodzimodzi ndi inu! Banja latsopano limene mulimo limatchedwa "mpingo." Onetsetsani kuwonetsa banja lanu la uzimu chikondi chochuluka.

### Scripture search

1. Baibulo limafotokonzera wotsatira a Yesu mosiyanasiyana. Fotokozani mawu atatu ofotokonzera wotsatira Yesu pa Machitidwe 11:26:

   a. ______________________________

   b. ______________________________

   c. ______________________________

2. Pakuti tiyenera kugwira ntchito pamodzi ngati Akhristu, mpingo nthawi zina umatchedwa ______________ (*1 Akorinto 12:27*).

3. Kodi mutu wa mpimgo ndi ndani? (*Aefeso 5:23*) ______________

4. Kodi ndi mchitidwe wotani umene ukutiwonetsa m'mene mpingo ulili wofunikira kwa Iye? (*Aefeso 5:25*) ______________

5. Kuti ndikhale mbali ya mpingo, ubale wake uyenera kukhala wotani ndi Khristu? (*Afeso 5:24*) ______________

6. Kodi makhalidwe anali wotani kumene Paulo anaphunzitsa za Moyo wake mwa Khristu? (*1 Akorinto 4:7*) ______________

7. Kodi ndi maphunziro ati amene Uthenga wabwino wa Yohane wa kuphunzitsani zokhudza mpingo?

   a. Kodi dziko lidzadziwa bwanji kuti ndine mbali imodzi ya mpingo owona (wophunzira wa Khristu)? (*Yohane 13:35*) ______________

   b. What special responsibility did Peter and all pastors who came after him have toward the church? (*John 21:16*) ______________

8. Werengani 1 Akorinto 11:23-26. Mpingo ukupitiriza kukondwerera mwambo uwu, wotchedwa "Chiyanjano" kapena "Mgonero wa Ambuye." Kodi timakumbukira chiyani tikamadya mgonero? ______________

9. Kodi ndiyenera kuchita motani ndi abale ndi alongo mu m'banja langa la mpingo? (*Agalatiya 6:2*) ______________

10. Pamene Mzimu Woyera apereka mphatso kwa munthu aliyense payekha, Kodi Cholinga chake ndi chiyani? (*1 Akorinto 12:4, 7*) ______________

11. SMipingo ina ndi yamphamvu Komanso yokonda, pamene ina ayi. Kodi ndi iti mwa mipingo iwiriyi imene uli ngati umene mungafune kuthandiza kuwupanga kapena kukhala wa m'menemo? (Onani umodzi.)

   ☐ a *Mpingo wa ku Yerusalemu (Machitidwe 4:32-33)*

   ☐ *b.* The church at Laodicea (*Revelation 3:14-17*)

12. Kodi machitidwe a Akhristu woyambirira ku chiphunzitso cha atumwi, chiyanjano, kunyema mkate komanso pemphero anali wotani? (*Machitidwe 2:42*) ______

13. Kodi ndifunika kusamalitsa chiyani ngati ndikufuna kukondweretsa Ambuye? (*Ahebri 10:25*) ______

## Mafunso anga a phunziro ili

______

## Zofunika kuchitapo kanthu

1. Kodi ndi mphatso zina ziti—kapena maluso ena—amene Mulungu wakupatsani Kuti mumange mpingo? ______

2. Kudzera m'chikhulupiriro chanu, munayanjanitsidwa kwa Yesu Khristu, ndipo mwa uzimu, kwa Akhristu ena onse. Muganizire kuchitapo kanthu kukayamba mpingo. Chiyanjano ichi ndichofunikira ndipo ndi ntchito yayikulu kuti Akhristu ayenera kuyanjana mwanjira ina iliyonse. Ndi thandinzo la mpingo wanu komanso abusa, mudzapitiriza kukula mwa Khristu. Zifukwa zina zimene ndiyenera kulowera mpingo ndi: ______

### Vesi loloweza

*Tiyeni tisaleke kusonkhana kwathu pamodzi monga mmene ena amachitira, koma tizilimbikitsana makamaka poona kuti tsiku la Ambuye layandikira. (Ahebri 10:25)*

## Zolemba zanga za uzimu

______

Mwachita bwino pakumaliza maphunziro! Masiku abwino ambiri akubwera pamene mukufunabe Mulungu!

# *Kuvomereza kwapadera*

________________________________________

DZINA

## Mwamaliza Maphunziro a Oyambilira a Baibulo a Achinyamata

____________________ M'BUSA

____________________ M'PHUZITSI

____________________ TSIKU

*Musalole kuti wina akupeputse chifukwa ndiwe wachinyamata, koma khalani chitsanzo kwa okhulupirira pa mayankhulidwe, pamakhalidwe, pa chikondi, pa chikhulupiriro ndi pa kuyera mtima.*

1 TIMOTEYO 4:12

# Mbiri ya kayendedwe

Dzina ______________________________

Keyala ______________________________

______________________________

______________________________

Tsiku ______________________________

| Nambala ya Phunziro | Tsiku lotembenukira mtima | Ndemanga |
|---|---|---|
| 1 | | |
| 2 | | |
| 3 | | |
| 4 | | |
| 5 | | |
| 6 | | |
| 7 | | |
| 8 | | |

## Phunziro 1

*Taonani ndayima pa khomo ndikugogoda. Ngati wina amva mawu anga natsekulachitseko, Ine ndidzalowamo ndi kudya naye, Ine ndi iyeyo.*

REVELATION 3:20

## Phunziro 2

*Palibe mayesero amene mwakumana nawo oposa amene anthu ena onse anakumananawo. Mulungu ngokhulupirika; sadzalola kuti inu muyesedwe koposa muyeso umene mutha kupirira. Koma pamenemwayesedwa, Iyenso adzakupatsani njira yopambanira mayeserowo.*

1 AKORINTO 10:13

## Phunziro 3

*Ndasunga mau anu mu mtima mwanga kuti ndisakuchimwireni.*

PSALM 119:11

## Phunziro 4

*Mpaka tsopano simunapemphe kalikonse m'dzina langa. Pemphani ndipo mudzalandira, ndipochimwemwe chanu chidzakhala chathunthu*

YOHANE 16:24

## Phunziro 5

*N'chifukwa chake chilichonse mungadye kapena kumwa, kapena chimene mungachite, chitani zonse ku ulemerero wa Mulungu.*

1 AKORINTO 10:31

## Phunziro 6

*Yesu anati, "Bwerani, tsateni Ine ndipo ndidzakusandutsani asodzi a anthu."*

MATEYU 4:19

## Phunziro 7

*Mulungu mwini, Mulungu wamtendere, akuyeretseni kotheratu. Mzimu wanu wonse, moyo ndi thupi zisungidwe zopanda cholakwa mpaka kubwera kwa Ambuye athu Yesu Khristu.*

1 THESSALONIANS 5:23

## Phunziro 8

*Tiyeni tisaleke kusonkhana kwathu pamodzi monga mmene ena amachitira, koma tizilimbikitsana makamaka poona kuti tsiku la Ambuye layandikira.*

AHEBRI 10:25